# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA

## NTHAMBI YOONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'ZINJA LA 2025-2026

## Chidule cha nyengo ya Dzinja ya 2025-2026

Katenthedwe ka Nyanja ya mchere ya Pacific sikakhudza kwambiri nyengo ya dzinja ya 2025/2026

M'boma la Likoma tiyembekezere mvula ya mlingo okhazikika mu dzinja la 2025/2026


## October 2025




Mwezi wa October ukuyembekezereka kudzakhala wotentha ndi wopanda mvula. Komabe, Tiyembekezere mvula ya Chizimalupsya ya mlingo osapyola 20mm.

Tiyembekezerenso mphepo ya mkutho ndi ziphaliwali m'mweziwu.


## November 2025




Tiyembekezere mvula ya mlingo okhazikika kapena yocheperapo yosapyola 50mm m'madera ambiri mu mwezi wa November.


Mvulayi ikuyembekezereka kudzakhala ya ziphaliwali ndi mphepo ya mkuntho.

## December 2025




Tiyembekezere mvula ya mlingo okhazikika m'mwezi wa December ku Chizumulu komanso ku Likoma. Mvulayi ikuyembekezereka kudzagwa ya mlingo wa pakati pa 150 ndi 200mm.
Mvula yokhazikika ikuyembekezereka kuyambira sabata lachiwiri la mweziwu.


## January 2026




Mvula ya mlingo wokhazikika kapena woposerapo, yosapyola 300mm, ikuyembekezeka kuzagwa m'boma la Likoma mu mweziwu.

Pali chiopsezo chachikulu cha ng'amba yosapyola sabata limodzi mu mweziwu.


## February 2026




Mu mweziwu, tiyembekezere mvula ya mlingo okhazikika.
Mvula yokwana 200mm ikuyembekezedwa kuChizumula pomwe paLikoma kukuyembekezedwa mvula yokwana 250mm.

Ng'amba yokwana sabata limodzi ikuyembekezereka m'mweziwu.


## March 2026




Mvula ya mlingo wokhazikika kapena woposerapo yokwana pakati pa 200 ndi 280mm ikuyembekezereka m'madera ambiri m'mweziwu .

Pali chiopsezo chachikulu cha ng'amba yosapyola sabata limodzi m'mweziwu.

## April 2026





Nyengo ya dzinja ikuyembekezeka kudzafika kumapeto m'mweziwu, pamene mvula yamlingo wosapyola 150mm ikuyembekezereka m'madera ambiri.

Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kudzafika kumapeto mu sabata lomaliza la mwezi wa April.

M'boma la Likoma tiyembekezere mvula ya mlingo okhazikika komansomlingo oposera okhazikika mu dzinja la 2025/2026. Mvula yobzalira ikuyembekezereka kuyambira sabata lachiwiri la mwezi wa December.
Palichiopsezo chang'amba yapafupifupi sabata imodzi mu mwezi wa January, February ndi March.
Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kudzafika kumapeto pofika sabata lomalidza ya mwezi wa April. Nyengoyi ikuyembekezereka kukhala ya masiku a pakati pa 130 ndi 140.

The table and figure below show monthly rainfall distribution for the season with a normal in grey.

| TUKOMBOCDSS | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 0.0 | 0.7 | 12.6 |
| NOV | 8.4 | 43.8 | 22.9 |
| DEC | 106.1 | 172.4 | 194.3 |
| JAN | 160.5 | 247.0 | 244.3 |
| FEB | 159.1 | 194.9 | 172.8 |
| MAR | 168.0 | 292.9 | 310.8 |
| APR | 57.2 | 144.6 | 188.9 |




**Ulosiwu udzaunikidwanso mu December 2025**

For further information contact: The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Zapangidwa ndi kusindikizidwa mothandizidwa ndi :